MaDiPHS

# MATENDA A KAFOTA WA NTHOCHI (bacterial Wilt)




Matenda a kafota
© DARS

**Kafota wa nthochi amayambitsidwa ndi kachilombo kosaoneka ndimaso kotchedwa bakiteliya (bacteria). Kachilomboka kamaononga nthochi potseka njira za madzi ndi michere zimene zimapangitsa kuti masamba a nthochi achite chikasu komanso afote ndipo izi zimachepetsa zokolola.**

**KUFALA KWA KAFOTA**

# Kufala kwa Kafota

## 1. Tizilombo tingathe kufalitsa Kafota



**Tizilombo monga njuchi timathandiza kufalitsa matenda a kafota**



## 2. Zipangizo zingathe kufalitsa Kafota



**Zipangizo monga mipeni, makasu zomwe zagwilitsidwa ntchito pa ntchochi yamatenda a kafota**



## 3. Kubzala nthochi yamatenda kale



**Kubzala nthochi yomwe yagwidwa kale ndi matenda a kafota**



Adopted © FOURTHWAY

# ZIZINDIKIRO ZA NANKAFUMBWE WA NTHOCHI



Nthochi zimapanga chikasu kuyambira masamba a m'mwamba ndipo amauma ngakhale m'nyengo ya mvula.



Mukadula thunthu, m'kati m'maoneka bulauni (brown) komanso mumatuluka fungo loipa.



Zipatso zimayamba kuwola zisanakhwime, nthawi zina zipatso zimatha kupsa bwinobwino koma mkati mwake muli molimba angakhale mutaiphika.

Thunthu la nthochi yamatenda likaviikidwa m'madzi, timadzi totsika kuchokera ku thunthu yoviikidwa timaoneka ngati mkaka

Some elements adopted © AFRICAN ORGANIC AGRICULTURE TRAINING MANUAL

## Kuthana ndi kafota




Adopted © FOURTHWAY

**Funsani alangizi azaulimi ngati mukufuna kudziwa zambiri**

**Malawi**
**Created/Edited on August 14, 2025**
© MINISTRY OF AGRICULTURE, MADIPHS PROJECT,
CC BY-NC-SA 4.0 LICENCE